PRESS RELEASE

CHENJEZO KWA NZIKA ZA DZIKO LA MALAWI PANKHANI YA MANKHWALA WOZUNGUZA BONGO

Unduna woona nkhani zakunja ndi mgwirizano wa dziko lino ndi maiko ena wati ndi wokhudzidwa ndi kuchuluka kwa milandu ya nzika za dziko lino maka-maka atsikana ndi amai omwe akuwamanga m'maiko ena chifukwa chopezeka ndi mankhwala wozunguza bongo. Mwezi wapitawu amai awiri anawamanga pa bwalo la ndege la Bole mu mzinda wa Addis Ababa m'dziko la Ethiopia chifukwa chopezeka ndi mankhwala wozunguza bongo woopsya kwambiri. Amai awiriwo akuwasunga ku ndende ina m'dzikomo podikilira kukayankha mlandu ku khothi. Mai winanso wa kuno ku Malawi anamulamula kukakhala ku ndende zaka zisanu ndi ziwiri m'dziko la Ethiopia pamene mai winanso wachinai akumuzenga mlandu m'dziko lomweli la Ethiopia atamugwira chaka chatha pa mlandu wonga womwewu. Palinso amai ena omwe ali ku ndende m'maiko a India ndi Latin America.

Malinga ndi zomwe afotokoza amai ambiri omwe akhala akugwa mu msamphawu, unduna woona nkhani za kunja ndi mgwirizano wa dziko lino ndi maiko ena, wapezanso kuti amai ambiri amawanyengelera kuti akawapezera ntchito kapenanso mabanja kunja kwa dziko lino pamene akapita m'maikowo amakawagwiritsa ntchito zonyamula mankhwala wosokoneza bongowo. Atambwali amenewa amanamiza amaiwa kuti ndi a bizinesi omwe awatengere ku maiko a India, Brazil komanso maiko ena akuzambwe muno mu Africa komwe amanama kuti ndi a bizinesi ya zodzola-dzola za amai komanso mesh mwa zina chikhalirecho atambwaliwa amagulitsa mankhwala wosokoneza ubongo monga cocaine, heroin ndi mankhwala ena woopsya wosokoneza bongo.

Amai ambiri mosadziwa amawanyamulitsa zikwama komanso sutikesi zotseka pamene akudutsa m'mabwalo a ndege poganizira kuti anyamula zodzola-dzola komanso mesh ya amai chikhalirecho mumakhala mankhwala wosokoneza bongo. Achitetezo m'mabwalowa amamanga amaiwo powaganizira kuti katunduyo ndi wao.

Kamba ka zimenezi, unduna woona nkhani zakunja ndi mgwirizano wa dziko lino ndi maiko ena ukuchenjeza nzika zake maka-maka amai kuti azionetsetsa kuti wina asawapusitse kuti amunyamulire ndikukapereka chikwama kapena katundu kwa anthu wosadziwika kunja kwa dziko lino kapenanso kuchita bizinesi kunja kwa dziko lino ndipo m'malo mwake akagwe mu msampha wonga uwu. Kuphatikiza apa undunawu ukuchenjezanso nzika za dziko lino maka-maka amai kuti asamalole munthu aliyense kuti aziwapatsira katundu kuti azikawaperekera kwa munthu woti sakumudziwa omwe angakumane nawo m'mabwalo a ndege komanso malo ena. Nkofunikanso kuti makolo azichenjeza ana awo komanso achibale omwe akuphunzira kunja kwa dziko lino paza mchitidwe woipa wa nzika za maiko ena zomwe zikugwetsa mavuto nzika za dziko lino.

Unduna woona nkhani zakunja ndi mgwirizano wa dziko lino ndi maiko ena ukuchenjeza kuti mchitidwe wopezeka ndi mankhwala wozunguza bongo ndi mlandu womwe wopezeka amalandira chilango kuphatikizapo chophedwa. Ndi udindo wa aliyense kuneneza munthu yemwe akumuganizira kuti akukhudzidwa ndi mchitidwe wogulitsa mankhwala wozunguza bongo m'dziko muno.

Chitetezo komanso kukonda dziko lathu ndi udindo wa aliyense m'dziko

Ministry of Foreign Affairs and International Cooperation
19th July, 2018